

“Mulungu Akuyang’ana Khalidwe”

Genesis 24:1,

“Ndipo Abrahamu anali wokalamba, ndipo anali wokalamba kwambiri mu usinkhu; ndipo Ambuye anamudalitsa Abrahamu mu zinthu zonse.”

Yesu amawerenga khalidwe osati mamembala. Kodi inu mukudziwa zimenezo? Iye amawerengera makhalidwe. Mulungu nthawi zonse wayesera kuti apeze munthu mmodzi mu dzanja Lake. Zonse zomwe Iye amasowa ndi munthu mmodzi, ndipo Iye adzachita ntchito yake. Kudutsa mu zaka ingoganizani: Iye akanakhoza kupeza munthu mmodzi yekha wolungama mu nthawi a Nowa. Mu nthawi ya Mose Iye anapeza munthu mmodzi yekha wolungama (*2 Mbiri 16:9*).

Mulungu akuyang’ana khalidwe, osati umembala, khalidwe. Eliyeza, pamene iye anapita kuti akapeze Mkwatibwi wa Isaki (*Genesis 24:1-9*), iye anatulutsa thukuta kufikira atapeza khalidwe. Kumbukirani, Abrahamu anamuika iye woyankhira monga Mulungu amatiyika ife woyankhira, ife azitumiki. “Kasakeni Mkwatibwi Wanga.”

Mulungu adalitse mtima wanu. Ine sindiri kuyang’ana mamembala; ine ndikuyang’ana angwiwo mu mtima, winawake yemwe adzakhulupilire Mawu (*Mateyu 5:8*).

Eliza anayang’ana, ndipo iye anaganiza, “O, ine sindingakhoze kuchita izi pandekha. Pali udindo ochuluka kwambiri. Ine ndikuzindikira udindo womupezera Isaki.....” chimene ndi choyimira cha mpingo, inu mukudziwa, Khristu, Rebecca, choyimira cha Mkwatibwi... Ndipo Eliyeza anagwada pa mawondo ake ndipo anati,: Mulungu, inu ingondithandizani ine.” Ndipo pamene iye anadzipereka kwa Mulungu, Mulungu anamuthandize iye. Iye anapeza Khalidwe.

Bwererani ku Mawu, mibale. Bwererani kwa Mulungu. Musati mupereke tcheru chirichonse ku mpingo uwu womwe inu mumasonkhanako. Inu mungakhoze kukhala kumeneko ngati inu mukufuna kutero, ngati iwo angakuloleni inu. Koma chinthu choyamba kuchita ndi kubwera kwa Mulungu. Ndiko kulondola.

Ndiyeno pamene Eliyeza anapeza khalidwe lomwe linali mwa Mkaziyo, Rebecca, Mkwatibwi wokongola wa Isaki, iye anamuza zokudza Isaki . ndipo Iye sanafunse konse kanthu kamodzi. Iye anakhulupilira Mawu, mthengayo, ndipo iye anapanga kukonzekera kuti apite(*Chibvumbulutso 19:6-8*). Ndipo iwo anapita, nawafunsa bambo, ndipo iye anati, ingofunsani iye; ndi namwali wa usinkhu, mfunseni iye, lolani chikhale chiganizo chake.” (*Genesis 24:57-59*).

Iye anati, “Ine ndipita.” Kwa ndani? Mamuna yemwe iye sanamuonepo konse. Sakudziwa kanthu ka iye (*1 Petro 1:8-9*). Komabe iye anali wokonseka, chifukwa iye anali wosankhidwiratu ndipo anakhazikitsidwiratu ku chimenecho, ndendende kulondola.

Inu mungathe kundimva ine ndikulalikira uthenga uwu. Inu mungathe kuwona Mzimu Woyera ukuzindikira zamitima ndi kuchita zinthu zazikulu ndi kuwonetsa zozizwa. Inu mungathe kupemphera, ndipo izo sizingafike pochitika konse. Pitiliranibe, mphotho yanu ibwera pa mapeto. Kodi izo sizidzakhala zabwino pamenepo? Inde. Mwawona, muchitireni Yesu ntchito. Ndiwo uthenga wa nthawi yotsiriza. Iye ali naye Mkwatibwi. Mulungu akuyang’ana khalidwe.

Ndiyeno atatha Eliyeza kupeza khalidwe, ndiye chinthu chotsatira chinali cha kumukonzekeretsa iye kuti apite. Ndi chomwecho tsopano, m’bale chomwecho tsopano. Uthenga wa nthawi yotsiliza suli kunja uko mu Babeloni. [1]

Mulungu nthawi zonse wakhala akuwerengera khalidwe, osati mamembala. Ndipo lero ife tachita mosiyantsa. Ife timawerengera mamembala, wovala bwino, wopereka bwino, malo mwa Khalidwe.

Eliyeza anatulutsa nthukuta, kufikira iye atapeza Khalidwe. Ndiko kulondola. Kodi Iye akanapeza ndani? Ndipo Iye anadalira Mulungu. Khalidwe la chiyani? Khalidwe kwa Isaki, Mkwatibwi, amene mpingo choyimira chake. Inu mukudziwa zimenezo. Iyo inali mbewu yachibadwa ya Abrahamu; iyi ndi mbewu ya Chifumu ya Abraham (*Agalatiya 3:7, 29*). Chabwino, ngati Eliyeza, Mthenga akusaka Mkwatibwi ndipo akuyesera

Kuti apeze Khalidwe, ngati mamuna ameneyo abwera, Mthenga wa tsiku lotsiriza, akuyesera kuti apeze Mkwatibwi wa Khristu, Iye sadzayang’ana pa Umembala wa chipembedzo. Iye adzayang’ana pa khalidwe lomwe liri lololera.

Penyani! Khalidwe labwino poyamba, kenako kumukonzekeretsa iye kuti akumane ndi Isaki. Atatha iye kupeza khalidwe, kenako kupangitsa iye kuyima chete motalikirapo mokwanira kuti amvetsere ku uthenga wake wa Isaki (*Yesaya 30:15, Salmo 23:2*).

Ameneyo ndi mthenga wa masiku wotsiriza, kuwala kwa kumadzulo, ziri koyamba kupeza mpingo umenewo (Ndikuti komwe iwo akakhulupilire uthenga?), kusake iwo. Saka komwe mpingo uwo uli womwe udzalole ngakhale iwe kulowa mkati, womwe sudzatseka chitseko pa nkhope yako. Ndiyeno pamene iwe uchita kumeneko, ndiye iwe wapeza khalidwe. Tsopano ngati iye adzayima chete motalikirapo mokwana kuti umuuze iye momwe Mkwatibwi uyo ayenera kukhala atavalira! Iye ayenera kuvekedwa. Imani chete!

Tayang'anani pa Rebecca wang'ono akumvetsera ku mawu aliwonse, mtima wake waung'ono unali kugunda. Iye anali kumuza. Tsopano, inu mwatulutsa nthukuta, "Ine ndidzapita kuti?" kufikira ine nditapeza khalidwe. Ndiye pamene ine ndapeza khalidwe, ndiye ndikupanga iye kuyima chete motalika mokwanira kuti akonzekeretsedwe iye kuti apite akakumane ndi iye. O, mai, ndi chinthu chokhudza bwanji! Kumakonzekeretsa iye; kuyima chete kuti amvetsere ku Uthenga wake wa Iye. Eliyeza sanali kuyankhula za iye mwini, koma iye anali kuyankhula za mmodziyo iye anatumidwa kuchokerako. Ndipo iye anali nazo mphatso kuti atsimikizire zoti iye anali atatumidwa kuchokera kwa iye. Amen! Iye amafuna kuti amveke iye ndi zinthu izi. Inu mukudziwa momwe iye anamuvekera iye.

Zindikira, mthenga wa nthawi yotsiriza, ntchito yake idzakhala kuti akakonzekeretse woyera mtima, Mkwatibwi kukonzekera Mkwati. Uwo udzakhala uthenga wake. [2]

Kukamba za Mamembala. Lero, zonse zomwe inumukufuna ndi mamembala, mamembala. Mulungu samayang'ana pa mamembala. Iye akusakasaka Khalidwe, kuti iye angakhoze kuyika Mawu Ake mwa Wina wake yemwe adzamukhulupilira iye. Monga ndinanena, usiku wina, Eliyeza anatulutsa nthukuta mpaka iye atapeza khalidwe la Mkwatibwi. Ndiye anayenera kuti amupange iye kuyima chete, n'cholinga kuti amumveke iye moyenera, kuti akakumane ndi mmodziyo iye anali kukamba za iye. [3]

Ine ndinati, Eliyeza anatulutsa nthukuta mpaka anapeza khalidwe mwa Rebecca. Ndiye anayenera kuti amumveke iye, kukonzekera, kumulora iye kuyima chete ndi kumvetsera pa Uthenga wake. Vuto la izo liri, lero, pamene inu mupeza Khalidwe, ziri zolimba kuti uwapange iwo kuyima chete motalikirapo kuti avale zovala ndi kuvekedwa. Ndiko kulondola. Ma Ricky ena ang'ono awakokera kale iwo mu njira yina. Ndiko kulondola. Koma pamenepo, Eliyeza anatulutsira nthukuta. [4]

Baibulo limati, “Mkazi Wake wadzipanga iye yekha kukonza” (*Chibvumbulutso 19:7*), pa mapeto a m’badwo. Ndi motani iye wadzipanga iye yekha kukonzeka, kuti akhale Mkazi Wake? Ndipo iye amachita. Chiyani? Ndi mtundu wanji wa chovala chomwe iye Wavala? Mawu Ake owe. Iye anavekedwa mu chilungamo chake (*Chibvumbulutso 19:8*). Ndizo zomwe. Izo ziri kulondola. Mwaona? [5]

Tsopano, tayang’anani kuno. Ine ndikuyembekezera iye adzaveke korona utumiki wanga wa izi, wondilora ine kutenga zovala za Mawu ndi kumuveka Mkwatibwi Wake mu zovala za Mawu ndi kwa chilungamo chake (*Akolose 3:10-15*). Ine ndikuyembekezera iye adzandiveke korona ndipo mundilole ine kuyima pamenepo pa tsiku limenelo, ndi kuti, “Tawonani Mwanawankhosa wa Mulungu amene akuchotsa tchimo la dziko lapansi.” (*Yohane 1:29*). [6]

Munthu amayang’ana kukogola kwachibadwa. Ndicho chinyengo. Ndicho chifukwa Mkazi anapatsidwa kukongola kumeneko, kwa chinyengo, kuti azinyenga. Mkazi wokongola, ngati iye sakugwiritsa iko mwa njira yoyenera, ndi themberero kwa iye; iko kudzamutumiza iye kugehena msanga koposa china chirichonse chomwe ndikuchidziwa. Ngati iye akhoza kukhala wokongola, ndithu, malingana ngati akhazikika ndi mamuna wake ndi kumachita chomwe chiri choyenera, ndicho chabwino ndi choyenera. Koma iye akhoza kutenga chinthu chomwecho ndipo, mai, momwe iye anganyengere nako, pakuti kunapatsidwa kwa iye kuti atero.

Zindikirani, tsopano, koma Mulungu amawonetseredwa mu khalidwe. “Munalibe Kukongola kuti tingamukhumbire Yesu,” (Yesaya 53:2-3), koma panalibe khalidwe monga lye, pa dziko lapansi.

Tsopano ife tikupeza, lero, kuti Khalidwe la Mpingo. Satana ndi gulu lake, amafuna matchalitchi akulu matchalitchi okongola, zinthu zokongola. Izo ndi zomwe dziko likuyang’anapo lero, “O, ndi abusa, nthawi yopambana yakuti-yakuti, zakuti-zakuti, Mwaunsembe chotero ndi mwa Umulungu, kuyenda atavala mikanjo yaikulu, ndi zinthu monga zimenezo.” Iwo amatcha kumeneko kukongola.

Koma woyera mtima enieni a Mulungu amafuna Khalidwe la Mawu otsimikiziridwa. [7]

Ndipo mu kuwazindikira iwo, ndiye ine ndinafika pamathero awa. Ziribe kanthu chomwe inu muli, Mulungu ayenera kupereka anthu omvetsera. Ndipo ziribe kanthu, ngati ine ndingakhoze kuyima pano mmawa uno ndi kubweretsa akufa ku moyo, ndi kubweretsa wolumala kuchikhalidwe chawo cha bwinobwino, ndipo apobe, Mulungu sali mu purogiramuso izo sidzipita kulikonse. Mulungu akuyenera kukhala mu purogiramu. Khalidwe Lake limadziwika mwa zintchito zake. Ziribe kanthu kuti iye ndindani, zintchito zake zimatsimikizira Khalidwe Lake.

Ngati inu mutenga munthu, ziribe kanthu mwabwino momwe iye amayesera kukhala, ngati zintchito zake ziri zoipa, ubwino wake wonse sufikira ku kanthu. Ndipo mawu a munthu ndilo khalidwe lake. Munthu amene mawu ake sali abwino, ndiye inu simudzakhala komwe ndi chidaliro mwa munthu ameneyo, chifukwa mawu ake siabwino. Chotero choncho Mulungu, Atate wathu, Khalidwe Lake ndi zintchito Zake zimatsimikizira chomwe lye ali. [8]

Ngati ine ndiri Mkhristu, ine ndikuyenera kuzindikiritsidwa ndi chitsanzo chirichonse cha Baibulo. Ine ndayenera kuyima ndi Nowa ndi kulalikirira ndi iye, mu masiku, ndi kuwachenjeza anthu. Ndiko kulondola. Ine ndayenera kuyima pa Phiri la Karmeli, ndekha, ndi Eliya. Ine ndayenera kuyima pa golgota, ndi kupachikidwa kwa ine mwini ndi maganizo anga omwe, ndi lye (Aroma 6:6). Koma ndiye kachiwiri, ine ndinawuka ndi lye pa Isitara, mwachigonjetso pamwamba pazinthu zonse. [9]

Mulungu khalani wachifundo pa ife. Ngati ife tiri ana amuna ndi akazi a Mulungu. Komabe ndife alendo mu moyo uwu. Mulungu akufuna Khalidwe kuchokera kwa amuna ndi akazi amene angakhoze kukhala khalidwe pawokha monga ana amuna ndi akazi a Mfumu. Mulungu khalani wachifundo pa ife, kuti ife tikachite izo.

Ndicho chomwe ndikuchisaka abwenzi: Khalidwe. Ndicho chomwe Mulungu ali akuchikokera, khalidwe kwa Mkwatibwi uyo yemwe adzatengedwe. Ndipo monga ana amuna ndi akazi a Mulungu, tiyeni tichite monga ilo; Khalani ana amuna ndi akazi! Mulungu tithandizeni ife.

[10

Chifaniziro:

[1] “Utumiki wa nthawi yakumapeto” (62-0603), ndime 193, 197-201, 213.

[2] “Mthenga Wakumadzulo” (63-0116), ndime 243-249.

[3] “Chizindikiritso” (63-0123), ndime 199-200.

[4] “Nthawi Imodzi yinanso, Ambuye” (63-0120 E), ndime 125.

[5] “Ululu Wakubala” (65-0124), ndime- 196.

[6] “Malo amene Utumiki wanga Wafika tsopano” (62-0908), ndime . 121.

[7] “Chikwati ndi Chirekano” (65-0221 M), ndime . 141-144.

[8] “Kukhulupilira Kuchokera mumtima” (57-0623), ndime. E-9.

[9] “Nthawi yokolola” (64-1212), ndime. 202.

[10] “Maumboni apanyanja” (62-0720), ndime. E-28.

Mwala womangira wauzimu No. 40: Kuchokera ku Mawu Owuluridwa a ora ino, Osindikizidwa ndi: Gerd Rodewald, Friedenstr. 69, D-75328 Schomberg, Germany

www.biblebelievers.de, Fax: (+49) 72 35 33 06

Kukubwera m’modzi ndi Uthenga umene wulunjika ku Baibulo, ndi mofulumira ntchito ya kuzungulira Dziko lonse. Mbewu idzalowa manyuzi pepala, Mu zipangizo zowerengera, mpaka mbewu yosankhidwiratu ndi Mulungu idzamva izo.

[M'bale Branham, "Mu Buku la Chikhalidwe- Dongosolo- Chiphunzitso cha Mpingo," Tsamba 724]